# Shire Valley Transformation Programme - 1

## 'Umoyo wabwino kudzera mu ulimi othilira wa mbewu zamalonda'







### Chiyambi cha Ntchito ya SVTP

Kuno ku Malawi, anthu ambiri amapeza ndalama ndi chakudya kudzera mu ulimi wa mbeu ndi ziweto. Ulimi umenewu umadalira mvula yomwe imagwa mosadalilika ndipo nthawi zambiri kumakhala chilala kapena madzi osefukila. Izi zimapangitsa kuti alimi azivutika kupeza chakudya chodyetsa mabanja awo ndi ndalama zotukulira pa khomo pawo ndiponso kukonza tsogolo la ana awo.



*Ulimi wa shuga kugwiritsa ntchito njira zamakono*

Kudzera mu pulojekiti ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP), Boma la Malawi likufuna kutukula ntchito za ulimi pothandiza alimi kuti azikolola zochuluka, azikhala ndi ziweto zathanzi, komanso azilima mbeu zopezetsa ndalama zochuluka zomwe angakagulitse ku misika.

Ulimi wanthilira umathandiza kutukula umoyo waalimi chifukwa mbeu zimakula bwino mosadalira mvula, alimi amakolola zochuluka ndipo ulimi wambeu zamalonda umapita patsogolo. Choncho, phindu la ulimi limachuluka komanso chakudya cha alimi ndi anthu onse chimapezeka mosavuta. Ndichifukwa chake Pulojekiti ya Shire Valley Transformation yakhazikitsidwa m'maboma a Chikwawa ndi Nsanje.

### Pulojekiti ya SVTP

Boma la Malawi kudzera mu Unduna wa Zaulimi ndithandizo lochokera ku Bank ya Dziko Lonse (World Bank), African Development Bank ndi Global Environment Facility (GEF), likuyendetsa pulojekiti ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP). Ntchito ya Pulojekiti ya Shire Valley Transformation ndiyazaka khumi ndi zinayi (14) kuchokera m'chaka cha 2018 mpaka mchaka cha 2031. Ntchitoyi igwiridwa mmagawo atatu otsogozana koma gawo lachiwiri lidzayamba loyamba lisanathe ndipo lachitatu lidzayamba gawo lachiwiri lisanathe.

Pulojekiti ya SVTP idzabweretsa madzi anthilira mudera lokwanira ma hekitala 43, 370 kuchigwa cha Mtsinje wa Shire kudzera mu chingalange kuchokera pa Damu la Kapichira m'Boma la Chikwawa mpaka ku Bangula, m'Boma la Nsanje. Izi zidzapangitsa kuti madzi othilirira mbeu adzipezeka chaka chonse mmadelawa.

Ndondomeko yoyendetsera Sikimuyi idzaonetsetsa kuti:

- ✓ Phindu la pulojekitiyi lakhudza anthu omwe ali ndi malo kapena akugwiritsa ntchito malowo kuti ayambe ulimi wamakono;
- ✓ Alimi amene ali ndi chidwi akhoza kugwirizana kuphatikiza malo awo pamodzi ndi kulima ulimi wanthilira;
- ✓ Ma kampani akutha kugwirizana ndi eni malo kuyambitsa ntchito zachitukuko;
- ✓ Anthu ali ndi mwayi wosankha kupanga nawo ntchito za Sikimuyi kapena ayi;
- ✓ Alimi akulipira ndalama pa madzi omwe akulandira kuti ndalamazi zizithandiza kuyendetsera Sikimuyi. Izi zidzathandiza kuti Sikimuyi idzapitilire mpaka muyaya.



*Malo amene padzayambire chingalande pa Damu la Kapachira*

## Cholinga cha Pulojekiti ya SVTP

Cholinga cha Pulojekiti ya SVTP ndi kutukula ntchito za ulimi kudzera muulimi wanthilira ndi kulimbikitsa malimidwe amakono kuti alimi ang'onoang'ono a mchigwa cha Mtsinje wa Shire adzipeza phindu. Cholinga cha Gawo loyamba la Pulojekitiyi (2018 mpaka 2023) ndikupereka madzi okwanira kupangira ulimi wanthilira, kuwonetsetsa kuti nkhani ya malo a ulimiwu ya unikiridwa bwino ndiponso malo osungila zachilengedwe akusamaliridwa ndi kutetezedwa.

## Chimene Pulojekitiyi Ikufuna Kukwaniritsa

- ✓ Kupereka madzi aulimi wanthilira modalirika, mundondomeko yalondolozeka bwino ndiyoyang'ana chitsogolo kwa alimi mwa magawo magawo komanso kupereka madzi ogwiritsira ntchito tsiku ndi tsiku;
- ✓ Kukhazikitsa magulu a alimi ang'onoang'ono omwe adzipanga ulimi wanthillira ngati bizinezi osati ulimi wongofuna kupeza chakudya chokha komanso kuwalumikizitsa ndi magulu amene ali okhazikika mu bizinezi;
- ✓ Kuthandizira mabungwe a alimi kukhazikitsa dongosolo logwiritsa ntchito malo lomveka bwino ndi kulimbikitsa ntchito zokhudza malo komanso kuphatikiza malo aulimi pamodzi;
- ✓ Kuonetsetsa kuti malo otetezedwa osungilako zachilengwedwe akusamalidwa.

## Omwe adzapindule ndi Pulojekiti ya SVTP

Cholinga cha Pulojekiti ya SVTP ndikuthandiza alimi ang'onoang'ono ndi alimi ena onse. Alimi okhala m'magulu ndi kugwiritsa ntchito malo ndi amene adzakhale oyamba kulandira madzi othilira mbeuwa. Anthu onse amene ali mmadera a pulojekitiyi adzalandira uthenga kuti asankhe ngati akufuna kupeza nawo mwayi oyamba ulimi wamakono wambeu zamalonda.

Pakuti pulojekiyi ithandiza anthu onse m'madera okhuzidwa, izi zidzatukula umoyo wa anthu popanda kusankha. Kalembera wa mchaka cha 2016 adayelekeza chiwerengero cha anthu amdera lokhudzidwa ndi Pulojekitiyi kuti ndi chokwana 279,550 kuchokera kumawanja 60,772.



*Alimi ang'onoang'ono ngati awa ndi amene adzapindule ndi ntchito ya SVTP*

## Madera Omwe Akhudzidwe

Ndondomeko yomanga Sikimu ya Shire Valley idzachitika m'magawo awiri. Gawo loyamba lidzakhudza dera la kumpoto kwa Boma la Chikwawa mpakana kumpoto kwa malo otetezedwa a Lengwe. Gawo lachiwiri ndi dera lakum'mwera kwa Lengwe mpakana ku Bangula m'Boma la Nsanje.

Pali malo amene sinaphatikizidwe nawo mu Sikimuyi ngakhale ali mdera limene chingalandechi chidzadutse. Zifukwa zake ndi izi:

- ✓ Malowo ali ku mtunda kuposera chingalande kotero kuti madzi a ulimi wanthilira ukuyenera kupopedwa kuti afikeko;
- ✓ Dothi la malowo ndilosagwirizana ndi ulimi wanthilira;
- ✓ Malowo ndi pamudzi pokhala anthu;
- ✓ Malowo ndi wotetezedwa pa zifukwa zina;
- ✓ Malowo ndi manda kapena malo otetezedwa okhudzana ndi za chikhalidwe.

## Chidzachitike ku malo a anthu n'chiani?

Pulojekitiyi imalemekeza ufulu wa anthu wokhala ndi malo. Anthu okhawo amene ali m'malo momwe chingalande ndi misewu zidzadutse adzasamutsidwa ndipo adzapatsidwa chipepeso. Anthu ena onse ayenera kudziwa izi:

- ✓ Minda ya nthilira idzakhazikitsidwa mbali mwa ngalande za madzi;
- ✓ Kudzakhala kofunika kuti alimi adzaphatikizane malo awo ndikupanga magulu a ulimi wa nthilira;
- ✓ Malire a malo adzasinthidwa pofuna kupeza malo a anthu omwe akulowa mu sikimuyi;
- ✓ Alimi adzayikidwa m'magulu kuti aziyang'anira madzi ndiponso, ngati kuli koyenera, ulimi wawo.

Pulojekiti ya SVTP idzathandiza kukonza migwirizano yosakakamiza pakati pa ma kampani ndi mabungwe a alimi. Izi zidzathandiza alimi kupititsa patsogolo ulimi wawo, kupeza misika yambiri ndi kulumikiza kagwiridwe ka ntchito za ulimi kuyambira ku munda mpaka kwa anthu ogwiritsa ntchito mbewu zochokera mu ulimi.

Kuonjezera apo, Pulojekitiyi idzathandizanso ulimi wa ziweto komanso kubweretsa madzi ogwiritsa ntchito za pakhomo ndi ntchito zina zing'onong'ono.

## Kukhazikitsa magulu a alimi ang'onoang'ono

Pali ndondomeko zokhazikika zimene alimi ang'onoang'ono amdera limene Pulojekitiyi ikugwira ntchito akugwiritsa ntchito poyendetsa minda yawo. Alimi aku Kasinthula ndi Phata ndi ena mwa alimi amene adakhazikitsa ndondomekozi pamene alimi a KAMA ali pakalikiliki wowonetsetsa kuti ndondomeko zoti zitsatidwe zili mmalo. Alimi amene akufuna kukhala nawo gawo la Sikimuyi akuyenera kubwera pamodzi, kusonkhanitsa malo awo ndi kulembetsa ku Boma.

Magulu a alimiwa ntchito yawo idzakhala yoyang'anira kuti minda ikuyenda bwino ndi kupanga migwirizano ndi Kampane imene Boma lidzalembe kuti idzayendetse Sikimu. Mgwirizanowu udzatsindika mtengo umene magulu alimiwa azidzapereka ku Kampane kuti izidzayendetsera Sikimuyi kuphatikizirapo kukonzera ngalande zikaonongeka komanso nthawi imene mgwirizanowo udzakhalire. Izi zidzathandizira kuti Sikimuyi adzakhale ndi phindu ngakhale kwa mibado ya mtsogolo.

## Ndondomeko ya Ulimi wa Makono/Ulimi ngati Bizinezi

Ulimi wanthilira umafunikira malo akulu kotero kuti alimi akuyenera kudzaika malo awo pamodzi nkupanga minda ikuluikulu. Alimi azidzalandira phindu/ndalama kutengera ndi kukula kwa minda yawo mbewu zikagulitsidwa komanso theka lina landalamazo lizidzasungidwa kuti lipitirire kugwira ntchito pa ulimiwo.

Alimi omwe ali ndi malo mkatikati mwama buloko amene adzapangidwe komanso madera ozungulira, ali ndi ufulu wopanga nawo ulimi wanthilirawu kapena ayi.



*Malo a chonde ngati awa adzagwiritsidwa ntchito ya ulimi wanthilira*

## Kodi Sikimuyi idzayendetsedwa bwanji?

Sikimu ya Shire Valley ndi zonse zoyenereza ulimi wanthilirawu ndi katundu wa Boma la Malawi. Boma lidzalemba ntchito Kampane imene idzakhale ikuyendetsa Sikimuyi.

Zina mwa ntchito ya Kampaneyi ndi izi:

- Kuonetsetsa kuti minda yonse ikulandira madzi okwanira monga mwa mgwirizano;
- Kuonetsetsa kuti ngalande ndi zonse zofunikira zikukonzedwa pafupipafupi kuti madzi apitirire kuyenda mofunikira;
- Kulowa mumgwirizano ndi magulu a alimi ndi kuonetsetsa kuti magulu a alimiwa akupereka ndalama zoyendetsera Sikimuyi mwazina.

## Kodi ndi mbewu ziti zimene zidzadzalidwe?

Cholinga cha Pulojekiti ya SVTP ndi kutukula alimi ang'onoang'ono a mchigwa cha Mtsinje wa Shire kuti adzilima ulimi wanthilira wamakono komanso wopindulitsa. Magulu a alimiwa adzasankha mbewu zimene adzafune kulima pa malo awo, koma mbewu zogulitsa kumsika yosiyanasiyana zidzalimidwa patheka lalikulu la mindayi.

Phindu lopezeka mu ulimi wanthilirawu lidzathandiziranso alimiwa kulipira Kampane yoyang'anira Sikimu. Theka lina la mindayi (10%) lidzagwiritsidwa ntchito motere; kulima mbewu zakudya, kudyetsera ziweto, ndi kubzala mitengo ya zipatso mwa zina.



Akadaulo azaulimi adachita kafukufuku wa mbewu zochuluka zimene zikhoza kulimidwa kudzera mu ulimi wanthilira ndipo zina zinasankhidwa kutengera kuti ndizosavuta kukula, kukolola, kusunga, kugulitsa komanso kupangira zinthu zosiyanasiyana.

Zina mwa mbewu zimene zinasankhidwa ndi chimanga, mzimbe chifukwa ndi mbewu imene imalimidwa kwambiri mderali, komanso zipatso zosiyanasiyana monga nthochi, mango, mapapaya ndi zina.

## Chipepeso

Boma la Malawi lidzayesetsa kuti anthu amene malo awo adzakhale nawo mgawo la kumangidwa kwa Sikimuyi alandira chipepeso choyenerera. Pali chiyembekezo kuti anthu ambiri sadzasamutsidwa chifukwa cha ntchitoyi.

Chipepeso chidzaperekedwa potsatira Malamulo a Dziko la Malawi, Malamulo a Banki ya Dziko lonse komanso African Development Bank. Ndondomeko yammene chipepesochi chidzayendere idzafotokozeledwa kwa anthu motsogozedwa ndi a Unduna wa za Malo.

Ntchito yomanga Sikimu sidzayamba mpaka chipepeso chitaperekedwa kwa anthu okhudzidwa. Madandaulo onse okhudzana ndi ntchito yomanga Sikimuyi akuyenera kuperekedwa ku makomiti amene anakhazikitsidwa mwa padera a mmudzi, a kwa T/A, a kwa DC komanso ku Boma.

Kuthetsa madandaulo kumudzi kudzathandiza kuti madandaulo onse awunikidwe ndi kuthetsedwa mwachangu kuopa kuchedwetsa ntchito za Pulojekiti pamene madandaulo atengedwa kupita ku khoti.

Anthu adzalandira chipepeso pa zinthu zamagulu awa:

- Malo;
- Zokolola monga mbewu, mitengo ya zipatso;
- Zomangamanga monga nyumba, matchalitchi, ndi masukulu mwa zina;
- Mitengo.

Anthu amene nyumba zawo kapena zomangamanga zina zidzakhudzidwe ndi kumangidwa kwa chingalande, adzapatsidwa mwayi wosankha kumangiridwa zina kapena kupatsidwa ndalama zamtengo wofanana ndi katundu amene adzagwetsedweyo.

Anthu amene malo awo ali mnjira ya chingalande koma pafupi ndi minda imene idzalimidwe adzakhala ndi mwayi ochita nawo ulimi wanthilira pamene anthu amene malo awo ali mnjira yachi ngalandeyi koma patali mindayi adzapatsidwa chipepeso.

Chipepeso chidzaperekedwanso kwa anthu amene adzaluze kholola lawo mminda komanso mitengo ya zipatso ndi nkhalango. Mtengo wa chipepeso udzatengela mtengo umene adatchetchera ndi kulambulira pa malopo poyamba ndi ndalama zimene munthu akanapeza pa nthawi ya khola. Nthawi imene Sikimuyi imajambulidwa, Boma linayesetsa kuyika misewu yodutsira anthu, ziweto komanso nyama zakutchire.

Pamalo pamene padzamangidwe Sikimuyi padzalambulidwa ntchito yomanga isanayambidwe. Ndikhumbo la Boma kupereka chipepeso ntchito yamanga chingalande isanayambe.

## Madandaulo

Boma kudzera mu Pulojekiti ya SVTP lidzayesetsa kuonetsetsa kuti madandaulo onse a anthu akumudzi amveka komanso kuthetsedwa. Anthu akhoza kukanena madandaulo awo ku ma Komiti apadera omva zamadandaulo akumudzi amene ali mderalo kapena ngati sakukhutira ku ma Komiti akwa Mfumu Yayikulu (TA kapena Paramount) kapena ku ofesi ya Bwanankubwa.

Pulojekiti idakhazikitsa ma komitiwa kuti amve ndikuthetsa madandaulo onse a anthu pankhani yokhudzana ndi pulojekiti mwachangu kuopa kuchedwetsa ntchito yomanga chingalande komanso kuti anthu akhale ndi mwayi wofotokoza madandaulo. Adindo onse a mmakomiti omva zamadandaulo adasankhidwa ndi eni ake akumudzi.

Makomitiwa adzalandira, kuunika, kufufuza komanso kuonetsetsa kuti madandaulo onse athetsedwa. Ngati madandaulo sanathetsedwe ndi komiti ya kumudzi, odandaula akhoza kukanena kukomiti ya kwa T/A kapena Paramount ndipo akalephera apo, akhoza kukanena madandaulowo ku komiti yapa Boma kudzera ku ofesi ya Bwanankubwa mpaka madandaulowo atathetsedwa.

Pulojekiti idzayesetsa kuti pasakhale chinyengo komanso kupondelezana pothetsa madanduwa.

## Ndondomeko yoyenera kutsatira pothetsa madandaulo

Munthu akapereka madandaulo, Komiti ya Kumudzi idzamva madandaulowo ndi kuyesetsa kuti afufuzidwe mwatsatanetsatane ndi kuthetsedwa mmasabata awiri. Koma ngati komitiyi yalephera, munthu ali womasuka kupititsa madandaulowo ku Komiti ya kwa Mfumu Yayikulu (TA) kumenenso madanduwo akuyenera kuwunikiridwa ndi kuthetsedwa kwa masabata awiri.

Ngati munthu sanakhutirebe akhoza kutenga madanduwo kupita nawo ku Komiti yapa Boma kudzera ku Ofesi ya Bwanankubwa kumenenso ndondomeko yake imatenga masabata awiri. Zikavutitsitsa madandaulowo akhoza kukasiyidwa pa Komiti yayikulu ya Dziko (National) kumenenso kumatenga masabata awiri. Ma komiti onsewa akakanika kuthetsa madandaulowo, munthu ali womasuka kupita kubwalo la milandu kukasuma.

Madandaulo onse adzalembedwa mbuku lapadera ndipo madandaulo onse operekedwa adzapezeka ku Ofesi ya Ulimi Wanthilira ku Khonsolo ya m'boma la Chikwawa ndipo anthu onse ndi omasuka kuwerenga.

Madandaulo onse okhudzana ndi nkhani zamalo akuyenera kuwunikidwa ndi makomiti (Land Tribunals) amene anakhazikitsidwa ndi Boma mugwirizana ndi Malamulo.

**Ngati muli ndi dandaulo lililonse lokhudzana ndi Pulojekitiyi, chonde kumanani ndi a komiti a mdera lanu kuti akufotokozereni ndondomeko imene mungatsatire kuti muthandizidwe'**

## Kusamala za Chilengedwe ndi Malo Otetezedwa

Ntchito yamamangidwe a chingalande idzayambira mkati mwa Nkhalango ya Majete. Boma lidzaonetsetsa kuti pomanga Sikimuyi zachilengedwe zidzatetezedwe. Chingalande chidzadutsa pansi mu nkhalango ya Majete kuti nyama zakutchire zizidzatha kudutsa komanso kuti alendo azidzathabe kukaona ku Kapichira. Malo amene chingalande chidzakhale chotsegula adzamangilidwa mpanda.



Boma lidzaonetsetsa kuti kayendedwe kamadzi pa Damu la Kapichira kasasokonezedwe chifukwa cha kumangidwa kwa chingalandechi. Mundime yachiwiri ya Pulojekitiyi, chingalandechi chidzadutsa munkhalango ya Lengwe. Mamangidwe a chingalandechi adzaonetsetsa kuti njira zodutsirapo nyama pokamwa madzi zilipo.

Boma ndi thandizo lochokera ku GEF, lidzaonetsetsa kuti zachilengedwe zikutetezedwa nthawi yonse imene Sikimuyi ikhale ikumangidwa. Malo otetezedwa azachilengedwe amene akhudzidwe ndi SVTP ndi Lengwe, Majete, Mwabvi, Elephant Marsh komanso Nkhalango ya Matandwe.

**Pulojekiti ya Shire Valley Transformation ikufuna kuzindikira mwapadera ma gulu awa chifukwa cha zithunzi zimene za sindikizidwa mbukuli:**

1. Khonsolo ya Boma la Chikwawa
2. Sikimu ya Nabomba ku Chikwawa
3. Illovo Sugar,Chikwawa
4. Issa Farms, Ngabu, Chikwawa
5. EGENCO
6. African Parks Majete

**Kuti mudziwe zambiri werengani pa intanet pa: www.svtp.gov.mw**

**Lembelani ku keyala iyi:**

Ministry of Agriculture
Shire Valley Transformation Programme,
16 Chilembwe Road,
P/Bag 379,
Chichiri,
Blantyre 3
Phone: **01 828 709**

**Kapena lembani kalata ya pa intaneti ku:**

Project Coordinator
Email: **projectcoordinator.doi@svtp.gov.mw**

Information Desk
Email: **info.doi@svtp.gov.mw**

**Kapena kafunseni zambiri ku Ofesi ya Ulimi Wanthilira imene ikupezeka ku Khonsolo ya Chikwawa**